Nanga ubwino wa kafukufukuyu ndiuti?
Sitikudziwa ngati kafukufufukyu akuthandizeni koma tikuyembekeza kuti mfundo zomwe tizipeze mu kafukufukufuyu zingathe kuthandiza kutukula moyo wa amayi mtsogolo. Nagti mutalowa mkafukufukuyu, tidzaonetsetsa kuti umoyo wanu uli bwino pokupatsani chithandizo choyenera.

Tingatani ngati pali chovuta kapena dandaulo

Madandaulo
Ngati mwakhudzidwa ndi china chiri chonse cha kafukufukuyu yankhulani ndi a dotolo kapena a namwino omwe akuona za kafukufukuyu kuti akuthandizeni. Ngati simukhutisidwabe mukhoza kufunsa a bungwe lomwe likuyendetsa kafukufukuyu. Mutha kudziwa zambiri za gululi kuchokera kwa a dotolo ndi anamwino omwe anakuthandizani.

Kupweteka/Kuvulala
University ya Birmingham idalonjeza kupereka chipepeso ngati mwapweteka pochita kafukufukuyu. Ngati mwapweteka chifukwa chosasamalidwa bwino muli ndi ufulu wopita ku khothi.

Chonde funsani akafukufukuyu ngati mukefuna kudziwa zambiri.

Kodi kutenga mbali mkafukufukuyu mkwachinsinsi?
Inde . Zotsatira zonse za kafukufukuyu zidzasungidwa mwachinsinsi. Zotsatira ziri zonse sizidzakhala ndi maina, zaka kapena address yanu. Ndipo zotsatira za kafukufukuyu zidzasungidwa bwino ku malo otetezedwa ndi a chinsinsi.

Maina anu sadzasindikizidwa mu zotsatira zakafukufukuyu. Ndi athu okhawo amene akuchita kafukufukuyu ndi amne akhathe kudziwa za inu.

Zotsatira za kafukufukuyu zidzatani?
Zotsatira za kafukufuku wa AIMS zidzakambidwa pa msonkhano womwe tidzachita komanso zizalembedwa mmabuku ena a chipatala (Medical journals) kapenanso pa lamya ya computer yotchedwa website (www.aimstrial.org) kuti anthu adziwe.

Adathira ndemanga pa za kafukufukuyu ndani?
Kafukufukuyu adavomerezedwa ndi a bungwe lotchedwa Ethical clearance committee of the College of Medicine (COMREC). Ili ndi gulu lomwe limaonetsetsa kuti kafukuffuku wachitika moyenera komanso odwala ali ndi chitetezo

Muli ndi mafunso ena?

Pamene mwawerenga ndi kukambirania ndi a kafukufuku tiri ndi chiyembekezo kuti mutenga nawo mbali mu kafukufuku wa. Ngati muli ndi mafunso muli oloredwa kutero Ndondomeko zonse zikupezeka kumapeto a kalatayi.

Mupasidwa katalayi komanso chivomerezo cha kafukufukuyu kuti musunge.

Zikomo kwambiri potenga nawo mbali mukafukufukuyu

Kodi mungatipeze bwanji?:
Chonde tiyimbireni foni nthawi ina iliyonse masana kapena usiku pa nambala iyi, **0882557379 or 0994286988.**

Membala wa kafukufuku mukhoza kumpeza masana pa nambala iyi **0882557379 or 0994286988.**

Tikupasani ma units a foni kuti musavutike potiyimbira foni ngati muli ndi mafunso ali wonse kapena mavuto aliwonse.

Tikupatsani ndalama zoyendera kuti mukabwerenso kuchitapala pakapita ma sabata awiri kapena ngati mungafune kubwera nthawiyi isanakwane.

Tidzakulondolani kuti tidziwe kuti muli bwanji komanso kukukumbutsani za tsiku lina lowonana nanu. Tikufunsani mutiuze momwe tingakupezereni.
Mmene tingakupezereni:
Dzina lanu:
Nambala ya foni yanu _____

Tikukuthokozani powerenga kalatayi ndi kutenga mbali mkafukufukufuyu

Version 1.0 Chichewa dated 21/03/2013

AIMS – Antibiotics in miscarriage surgery

Participant Information Sheet

Mukuitanidwa kuti mulowe kutengapo mbali mu kafukufuku. Musanapange chisankho cholowa mukafukufukuyu muyenera kudziwa cholinga chakafukufukuyu komanso zofunika kuchita pa kafukufukuyi.

Tikufuna kuona ngati mankhwala opha tizilombo (a antibiotic) angathandize kuchepetsa matenda omwe angathe kubwera chifukwa chopangidwa opereshoni yotsukidwa mmimba mimba itachoka. Kafukufukuyu akutchedwa AIMS Trial.

Chonde funsani mafunso ngati pali chilichonse chomwe simukuchimvetsa kapena kuti mudziwe zambiri. Kafukufukuyu akuthandizidwa ndi University ya Birmingham, kuulaya (United Kingdom). Ndalama zakafukufukuyu zachokera ku bungwe la Medical Research Council, United Kingdom, the Wellcome Trust ndi ku Department ya International Development, United Kingdom.

UNIVERSITY OF BIRMINGHAM

SAMPLE

Mwachidule

Matenda amimmba (pelvis) obwera kamba kopangidwa opereshoni yotsuka mmimba pamene mimba yayochoka akhoza kubweretsa mavuto ochuluka pa moyo wa mayi.

Mmaopereshoni a mitundu ina, mankhwala opha tizilombo (antibiotic) omwe amaperekedwa opereshoni isanachitike atha kuchepetsa chiopsezo cha matenda pa odwala.

Komabe sizikuziwika bwino lomwe ngati izi zingathandize pa opereshoni yotsuka mimba ichi ndi chomwe chifukwa chake kofunikira kuti kafukufuku wa AIMS akufunitsitsa kupeza mayankho.

Tikupempha amayi omwe akufuna kuchitidwa opereshoni yotsuka mimba kuti alowe mukafukufukuyu. Theka la amayi oyenera opereshoni adzpatsidwa mankhwala opha tizilombo (a antibiotic) (Metronidazole ndi Doxycycline) muyeso umodzi maola awiri opereshoni isanachitike ndipo theka lina la amayi lidzapatsidwa mankhwala ongofanizira chabe. Mankhwala ongofanizirawo amaoneka ngati ndi eni eni koma mphamvu zawo ndi zocheperako.

Cholinga cha kafukufufukyu ndi chiyani?

Cholinga cha kafukufukuyu ndi chofuna kudziwa ngati kupereka mankhwala opha tizilombo a antibiotic kwa amayi asanachitidwe opereshoni kungathandize kuchepetsa chiophyezo cha matenda otsatira opereshoni. Makhwala opah tizilombo a antibiotic ake ndi Doxycycline 400mg ndi Metronidazole 400mg.

Ndaitanidwa chifukwa chiyani?

Mwaitanidwa kutenga nawo mbali mukafukufukuyu ngati mukuyenera kuchitidwa opereshoni yotsuka mmimba mimba itachoka.

Kodi ndikokakamiza kulowa mukafukufukuyu?

Ayi. Zili kwa inu kulowa kapena kusalowa mukafukufukuyu. Ngati mungafune kutenga mbali, mupatisdwa fomu kuti musunge komanso ku saina fomu yovomereza (Consent). Muli ndi ufulu wosiya kutenga nawo mbali nthawi ina iliyonse popanda kupereka chifukwa komanso izi sizizakhuza chisamaliro chanu ayi.

Chingatitike nchiani ngati mwalowa mkafukufukuyu?

Ngati mwapanga chisankho cholowa mukafukufukuyu ndi ku saina fomu yovomereza (Consent) mudzayenera kupatsidwa ndi wakafukufuku mankhwala oyesedwa maola awiri opereshoni isanachitike. Mankhwala opha tizilombo antibiotic ndi ena ofanana nawowa amaoneka chimodzimodzi kotero kuti inuyo ndi akafukufukuyu simudzaziwa kali konse. Mudzalandira ma tabuleti asanu onse pamodzi omwe mudzameze ndi madzi.

Mudzayenera kuchitidwa opereshoni monga mwachikonzero (pokhapokha ngati padzakhale chifukwa chosachitira opereshoniyi). Kutenga mbali sikungasinthe china chilli chonse pa opereshoni.

Muyenera kudziwitsa dotolo kapena namwino wokuyang'anirani mutapezeka ndi vuto liri lonse kutsatira opereshoniyi. Ngati muli ndi vuto liri lonse musanapite kunyumba dziwitsani namwino kapena dotolo amene akukuyang'anirani. Ngati mutapeza vuto masabata awiri asanathe chonde tidziwitseni ndipo tidzakuonani mwasanga. Nambala ya foni yathu ili mmunsi mwa kalatayi.

Ngakhale kuti muli bwino tikupemphani kuti mubwerenso patapita ma sabata awiri kutsatira opereshoni kuti tizakuoneni. Ngati muzabwere ndi vuto kutsatira opereshoni tizakupimani magazi kuti tione ngati muli ndi zizindikiro za matenda aliwonse. Ngati mungapezeke ndi matenda ali wonse, tizakupimanisano bwino bwino kuti tikupaseni mankhwala oyenera.

Ndingachite chiyani ngati nditapangidwa opereshoni?

Chonde tidziwitseni ngati mutaona zizizndikiro izi pasanapite masiku khumi ndi anayi (14) mutachitidwa opereshoni:

- Kupweteka pansi pa chombo
- Kutentha thupi, kuzizira kapena kunjenjemera
- Chikazi chili chonse chodwabwitsa kapena chafungo
- Kutaya magazi njira ya abambo kapena zowondana
- Kuphwanya thupi
- Matenda a pa khungu kapena zotupa
- Kapena vuto lina liri lonse

Nkhaniyi ikupezekaso mu khadi ya kalondolondo

Ndi mankhwala ati omwe akuyesedwa?

Mankhwala omwe akuyesedwa ndi Doxycycline (400mg) ndi Metronidazole (400mg). Mankhwalawa akhala akugwiritsidwa ntchito kuchiza matenda mmimba pansi pamchombo (pelvis) komanso mu maopereshoni ena. Mankhwalawa amagwira bwino ntchito ndipo alibe zotsatira zoipa.

Kodi kuipa ndi kuopsa kwa kafukufukuyu ndikuti?

Mutha kusapeza bwino pang'ono ndi Doxycycline kapena Metronidazole, koma izi sizichitika kawirikawiri. Ngati mupeza vuto chifukwa cha chithandizo cha mankhwalawa uzani adotolo kapena anamwino omwe akuthandizani mwa msanga.

SAMPLE